cepa
Centre for Environmental Policy and Advocacy

July 2021
Vol. 19. Issue 1.

# TIYENI TITENGE MBALI POTETEZA NKHALANGO ZATHU



Munkhalango za ku Malawi muli mitengo yosiyanasiyana ya chilengedwe, kuphatikizapo ina yosowa monga m'bawa ndi Mulanje Cedar, yomwe imapezeka ku Malawi kokha kuno.

- Mitengotu imatengulira chikhalidwe ndi umoyo wa anthu, imapititsa patsogolo chuma cha dziko ndipo imapangitsa kuti zamoyo zina zipeze mphweya, zakudya ndi nthuzi zomwe zimapangitsa kuti moyo ukhale tayale.
- Mitengo ndi chuma cha dziko ndipo iyenera kupindulira aliyense. Ngakhale zinthu zili chomwechi, mchitidwe odula mitengo ndi cholinga chootcha makala ukuchepetsa chiwerengero cha mitengo ndi miyoyo ya za chilengedwe zina, zomwe ziri zomvetsa chisoni.
- Tili ndi udindo oteteza mitengo ndi zachilengedwe zonse zobiriwira kuti mavuto odza kamba ka kusintha kwa nyengo monga kusefukira kwa madzi achepe.
- Udindo oteteza za chilengedwe ndi wa tonse.
- Mwa zina, tipewe kudula mitengo mwa chisawawa ndi kuotcha makala osavomelezeka ndi boma.

## Phindu La Mitengo

Mitengo ndi nkhalango ndi maziko a chuma cha dziko komanso chikhalidwe cha anthu. Mwa zina, akasupe ambiri amapezeka kumene zachilengedwe monga mitengo sizinadulidwe kwambiri, ndipo mabungwe ogawa madzi amatenga madzi awo ku madera omwe mitengo ndi nkhalango sizidasakazidwe. Matabwa, zipatso, nkhuni, mankhwala a zitsamba, nyama za kuthengo, a gulugufe, njuchi ndi tinyama tina tomwe timapangitsa kuti mbewu zipange maluwa; zonsezi gwero lake ndi mitengo. Kuphatikiza apo, mitengo imakongoletsa dziko ndipo imapereka nthuzi pamene anthu akuchita mwambo osiyanasiyana. Tisayiwalenso kuti mitengo imatsuka mpweya oyipa ndipo mitengo ina monga nsangu imabweretsa chonde mu nthaka ndipo imathandiza kuti nyengo ikhale m'chimake.

Dziwani kuti nkhalango zambiri zowirira m'dziko muno zimapezeka m'malo otetezedwa ndi malamulo komanso oyendetsedwa ndi mabungwe, ndi anthu. Kawirikawiri, malowa amazunguliridwa ndi anthu amene amadalira zinthu zopezeka m'nkhalangozi pa moyo wawo wa tsiku ndi tsiku.


## Mitengo Ndi Nkhalango Zikusakazika

Mfundo za chitukuko za dziko lonse zimalimbikitsa mizinda kukhala ndi malo osungirako mitengo, udzu ndi zomera zina zobiriwira ngati njira imodzi yotengulira moyo. Mwa zina, adindo ali ndi udindo oteteza za chilengedwe ndi kubwezeretsa zachilengedwe zosakazidwa.

# Mitengo Ndi Nkhalango Zikulakatika

Mitengo imatipatsa nkhuni zophikira komanso kubweretsa kufunda mu nyengo yozizira. Mawanja 97 mwa 100 aliwonse ku Malawi kuno amadalira makala opangidwa ndi anthu opanda chiphaso chowavomereza. Mmadera a m'matauni, anthu 76 mwa anthu 100 aliwonse amagwiritsa ntchito makala pophika ndi ntchito zina, chonsecho makalawa amapangidwa mosatsata malamulo. Kukula kwa chiwerengero cha anthu kwapangitsa kuti zachilengedwe zikhale pa mpeni, popeza mitengo imene ikugwetsedwa ikuposa imene ikubyalidwa chaka ndi chaka. Zimenezi zikuyika pa chiopsezo mibadwo ya kutsogolo popeza dzikoli ndi losiyirana. Ena mwa mavuto amene angadze kamba kosasamala za chilengedwe ndi monga kusowa kwa chakudya .Paja amati mubvi oyang'anira suchedwa kulowa m'maso, tikuyenera kugwirana manja poteteza za chilengedwe zimene zatsala kuti tisazanong'oneze bondo.

**Kodi anthu a m'tauni amagwiritsa ntchito chiyani kuphikira chakudya?**



# Chatsitsa Dzaye Kuti Njobvu Ithyoke Mnyanga

Ngati mumakhala m'tauni, ndipo mumagwiritsa ntchito mbaula; simuli nokha, popeza anthu 76 mwa anthu 100 aliwonse amagwiritsa ntchito makala pophika komanso kutenthetsa pa malo.

Pakati pa zaka za 2011 ndi 2018, chiwerengero cha anthu amene akugwiritsa ntchito makala chinakwera kuchoka pa six (6) mwa anthu 100 aliwonse kufika pa 18 mwa anthu 100 aliwonse. Chodetsa nkhawa ndi chokuti, mu nthawi yomweyi, chiwerengero cha anthu ogwiritsa ntchito makala m'matauni chinakwera kuchoka pa 42 kufika pa 76 pa anthu 100 aliwonse. Zotsatira zake ndi zokuti mitengo yambiri ikugwetsedwa ndipo vuto la kukokoloka kwa nthaka lakhudza dziko lonse.




**Pamagwetsedwa mitengo yambiri kuti patuluke thumba limodzi la makala**

## Zotsatira Za Kudula Mitengo Mwa Chisawawa

Mwa zina, mchitidwe odula mitengo mosasamala wabweretsa mavuto awa:


- **Kuchepa kwa zokolola.** Kudula mitengo mwachisawawa kwapangitsa kuti nthaka idzikokoloka mosavuta. Nthaka ikamakokoloka, chonde nacho chimathawa, zimene zimapangitsa kuti zokolola zidzikhala za m'manjamu. Nthaka yokwana matani 29, omwe ndi makilogalamu zikwi 29,000 ikukokoloka chaka ndi chaka ku Malawi kuno. Nako kusadalirika kwa mvula, kamba ka kuchepa kwa mitengo, kwapangitsa kuti mvula idzikhala ya njomba ndipo anthu asamakolole zochuluka. Pakadali pano, dziko la Malawi likumataya ndalama zokwana K50 biliyoni pa chaka kamba kokolola chakudya ndi zomera zochepa. Ndalama zimenezi zikadathandiza kwambiri alimi, m'dzika za dziko lino ndi anthu ongobwera ndipo zikadatukula chuma cha dziko.

- **Kuchuluka kwa mavuto okudza kamba ka kusintha kwa nyengo:** Mchitidwe odula mitengo mwa chisawawa wapangitsa kuti nthaka izikhala pa mtetete. Mvula ya mphamvu ikagwa, nthaka imakokoloka mosavuta, zimene zapangitsa kuti vuto losefukira kwa madzi lifike pampondachimera. Madzi othamanga komanso osefukira apangitsa kuti zidikha ndi mitsinje zizidzadza mwachangu, zimene zapangitsa miyoyo ndi katundu wamnanu kusakazika. Anthu okhala kufupi ndi mapiri, awa ndi monga a ku tawunishipi ya Chilobwe ku Blantyre ndi Ntandire ku Lilongwe, akukhalira mphanthi. Amayi ndi amene akuvutika kwambiri ndi mavuto odza kamba ka kusintha kwa nyengo, popeza amayenda mtunda wautali kuti apeze madzi okumwa ndi ogwiritsa ntchito za pakhomo, mwa zina.



Kudula mitengo kumaonjezera kuthamanga kwa madzi amvula ndi kukokoloka kwa nthaka yomwe ili pachitetete.

- **Kuzimazima kwa magetsi:** Dziko la Malawi limadalira kwambiri mphamvu za magetsi zochokera ku madzi. Komatu ntchito zogawa magetsi zasokonekera popeza matope okokoledwa ndi madzi othamanga akumalowa m'zipangizo zopangira magetsi oyendera mphamvu ya madzi ndi kupangitsa kuti bungwe logawa magetsi lidzinyetsula myetso [loadshedding pa Chingerezi]. Zimenezi zapangitsa kuti ntchito za magetsi zilowe pansi popeza magetsi akumazimazima. Kuzimazima kwa magetsi kwapangitsanso kuti anthu azigwiritsa ntchito makala osavomelezeka, zimene zapangitsa kuti mitengo isakazike m'dziko muno.



ESCOM — Electricity Supply Corporation of Malawi Ltd

egenco — Electricity Gebereation Company (Malawi) Ltd

**PRESS RELEASE** 7th March, 2019

**CURRENT STATUS OF POWER GENERATION AND SUPPLY IN THE COUNTRY**

The Electricity Supply Corporation of Malawi (ESCOM) Limited and the Electricity Generation Company (Malawi) Limited (EGENCO) wish to inform the general public that the hydro power generation has reduced due to excessive trash which has blocked intake screens at Nkula and Kapichira power stations as a result of heavy rains.

- **Tsogolo la ana anthu liri pa chiopsezo:** Ngakhale nkhalango zina ndi zotetezedwa m'dziko muno, mchitidwe odula mitengo mokuba wachuluka, makamaka m'mizinda ya Blantyre, Zomba, Lilongwe, ndi Mzuzu, zimene zapangitsa kuti nthaka yomwe m'mbuyomo idatchingidwa ndi mitengo ikhale pa mbalambanda. Zinthu zifika poyipa tikapanda kuchepetsa kapena kuleka mchitidwe odula mitengo mwachisawawa, makamaka pofuna kupangira makala osavomelezeka. Tangoganizani kukwera phiri lopanda mitengo. Sizingakhale bwino. Mitengo imapangitsa kuti mapiri azioneka okongola.

# Malamulo Amati Chiyani?

Malamulo oyendetsa za nkhalango m'dziko muno, aja amati National Forestry Act, amanena kuti za chilengedwe ziyenera kutetezedwa, kubwezeretsedwa, maka maka m'madera amene zachilengedwezi ziri pa chiopsezo, kuti umoyo wa anthu usasokonekere. Zina mwa zoletsedwa malingana ndi malamulowa ndi:

- **Kudula, kuzula, kukolola ndi kutenga zachilengedwe kuchoka m'malo a boma;**
- **Kulima mbewu, kudyetsa ziweto, kupalira, kukumba malo oyikidwa padera ndi cholinga chopanga chitukuko monga cha misewu ndi ntchito zina;**
- **Kuyang'ana ndi kukumba miyala ya mtengo wapatali m'malo otetezedwa;**
- **Kumanga nyumba komanso kukhazikitsa malo osungira ziweto m'malo otetezedwa;**
- **Kutaya zinyalala ndi zinthu zina m'malo otetezedwa, kaya ndi mu nkhalango kapena midzi yokhala mphepete mwa nkhalango kapena mu nkhalango imene;**
- **Kuotcha makala popanda chiphaso kapena chilolezo kuchokera ku Nthambi ya za Nkhalango;**

**Pajatu anthu ndi mabungwe okhawo amene ali ndi chiphaso kuchokera ku Nthambi ya za Nkhalango ali ololedwa kuotcha makala. Onse onyozera amalipiritsidwa chi ndapusa cha ndalama za pakati pa MWK500,000 ndi K10 miliyoni komanso kukagwira ntchito ya kalavulagaga kwa zaka za pakati pa chimodzi ndi makumi awiri [20].**

## Kunyozera Sikupindula

Komatu, ngakhale malamulo okhwima alipo, vuto lagona posagwiritsa ntchito malamulowo, makamaka pamene ophwanya malamulowo agwirizana ndi ogwira ntchito za nkhalango ndikudula mitengo mwachisawawa. Anthu enanso amatengera dzibwana malamulo oteteza nkhalango, zimene zikuyika za chilengedwe zathu pa mpeni (chiopsezo).

# Tingachite Chiyani?

Komatu madzi sadatayike onse, popeza tikhoza kuchitapo kanthu. Mwa zina, tingathandizepo poteteza zachilengedwe pochita zotsatirazi:

- **Yambani kugwirisa ntchito njira zamakono pophika.** Masiku ano, kuli njira zambiri zophikira kapena kutenthetsera zinthu popanda kugwiritsa ntchito makala ndi nkhuni. Mwachitsanzo, tiri ndi magetsi a mphamvu za mbwelera, a mphamvu zomwe sizambwerera, mphamvu za madzi, zinyalala zokwiririka mu nthaka ndi zina. Tikhonzanso kugula makala kwa anthu amene ali ndi ziphaso.
- **Kanenezeni** anthu owononga za chilengedwe ku nthambi zokhazikika kuti azengedwe milandu
- **Anthu ogwira ntchito zoteteza** za chilengedwe awonetsetse kuti anthu ophwanya malamulo alandira chilango choyenera.
- **Tipereke zipangizo zoyenera** kwa anthu amene amaotcha makala mosatsata malamulo kuti apeze njira zina zopezera ndalama. Anthu akhoza kuphunzitsidwa usodzi, ulimi wa njuchi, ulimi wa



mitengo ya zipatso komanso ulimi wa khofi, mtedza wa macademia ndi zina

- **Tibzyale mitengo ndi kuyisamala,** makamaka mu nyengo yobyala mitengo yokhazikika m'dziko muno. Amalawi amapemphedwa kubyala mitengo mu nyengo ya mvula kuyambira mwezi wa November mpaka March. Pajatu njere za mitengo sizigulitsidwa pa mtengo oboola mthumba ndipo zingagulidwe ndi K100 yokha basi njere imodzi. Popeza kuthyola khobwe ndi m'mawa, tidziyamba kukonzekera ntchito yobyala mitengo posungiratu njere mu nyengo ya chilimwe.



*Uthengawu wakonzedwa pansi pa ntchito ya Tiphike Mwa Makono Poteteza Nkhalango (Modern Cooking for Healthy Forests in Malawi") ndi chithandizo chodzera ku mabungwe a USAID ndi UKaid.*

*[BLANK]*



**The Centre for Environmental Policy and Advocacy, CEPA,** is a Malawian civil society organisation that advocates for environment and natural resources policies to be implemented for sustainable development.

**Info@cepa.org.mw / www.cepa.org.mw**

USAID
KUCHOKERA KWA ANTHU AKU AMERICA

UKaid
from the British people